Candidate Name:_________________________________________

# MACHINGA BOMA ZONE EXAMINATION COMMITTEE

2022/2023 END OF TERM ONE EXAMINATION FOR STANDARD 6

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

Tsiku:_____________________ Nthawi:__________

Dzina la Ophunzira: ________________________________________________________________________
**(la bambo koyamba)**
Dzina la Sukulu: __________________________________________________________________________

**Malangizo:**

- **Pepala ili lili ndi masamba 5 chonde yang'anani**
- Lembani dzina lanu pa tsamba lililonse
- Pepalali lili ndi magawo anayi A, B, C ndi D
- Yankhani funso limodzi mu gawo A ndi mafunso onse m'magawo otsatira. Mu gawo D, zungulizani lembo A, B, C kapena D posonyeza yankho lolondola

## GAWO A: (malikisi 30)

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso omwe ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu: **GULE WAKWATHU**

Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu:

**Ndime yoyamba**

- Dzina la gule yemwe amavinidwa kwanu.
- Anthu omwe amavina guleyu
- Nyengo yomwe guleyu amavinidwa

**Ndime yachiwiri**

- Zovala zomwe zimavalidwa povina guleyu.
- Zifukwa zovinila guleyu
- Ubwino wa guleyu

**Ndime yachitatu**

- Momwe mukulimbikitsa guleyu kuti apitilire.

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa makoloanu yopempha ndalama zolipirira ulendo womwe sukulu yanu yakonza wokawona nyama kunkhalango ya boma. Mwa zina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**

- Dzina la nkhalango komwe mudzapite
- Tsiku la ulendowo
- Ndalama za ulendowo

**Ndime yachiwiri**

- Zomwe mukuyembekezera kukaona
- Kufunika kwa ulendowo pamaphunziro anu.

**Ndime yachitatu**

- Chisangalalo chomwe muzakhale nacho mukadzapita nawo.

Candidate Name:_______________________________________

Candidate Name:________________________________________

**GAWO B ( Malikisi 20)**

**KUMVETSA NKHANI**

3. Werengani nkhani yotsatilayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

M'mudzi mwa a Chaisa mudali mkulu wina dzina lake Therapansi. Mkuluyu adali ndi ana a amuna awiri. A Therapansi adali otchuka kwambiri m'mudzi onse chifukwa adali pwepwete.

Tsiku lina bamboyu adadwala kwabasi. Chibayo ndi chimene chidavuta. Mauthenga adapita kwa abale komanso kwa a sing'anga omwe amawathadiza akadwala nthawi zonse. A sing'anga adawatema mphini kudzungulira nsana onse. Ngakhale a Therapansi adali akuthatha ndi imfa, adali kudera nkhawa ana awo omwe sadamvere malangizo.
Tsiku lina adazutsa mutu akubuula nati "kodi ana anga ali kuti? " Panthawiyo anawo adali nyumba momwemo, ndipo adasendera pafupi kuti amvetsere zomwe anene. Bamboyo adati "Ine posachedwapa nditsikira kuli chete. Inuyo simudafune kumvera malangizo anga. Mukhala moyo waulesi, wa uchidakwa ndi wa chifwamba. "
Atayankhula mawuwa adatsinzina ndipo womwewo mpaka osadzukanso.

**Tsopano yankhani mafunso awa:**

a. Kodi pwepweteyu amakhala kuti?
________________________________________ (malikisi 2)

b. Mkuluyu adali ndani?
________________________________________ (malikisi 2)

c. N'chifukwa chani adaitanitsa a chibale?
________________________________________
________________________________________ (malikisi 2)

d. Tchulani matenda omwe bamboyo amadwala?
________________________________________ (malikisi 2)

e. Kodi ana abamboyo samammvera chiyani?
________________________________________ (malikisi 2)

f. Perekani zosatila dziwiri zakusamverako
____________________ ____________________ (malikisi 2)

g. Perekani matanthauzo amawu otsatirawa:
(i) pwepwete: ________________________________________
(ii) Kutsirira kuli chete: ________________________________________ (malikisi 2)

h. Perekani chikhulupiriro chimodzi chomwe mkuluyu adali nacho akadwala.
________________________________________ (malikisi 2)

i. Perekani mutu wa nkhaniyi.
________________________________________ (malikisi 2)

**GAWO C (MALIKISI 10)**

4. a. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.
“Chaka chino ndaganiza mozama. Ndikufuna tonse tibzale mbewu yamakono ya chimanga kuti m'mudzi muno musadzadutsenso galu wakuda.”

**Mafunso**

i. Ndi malonje anji amenewa?
________________________________________(malikisi 1)

ii. Kodi malonjewa akuyankhulidwa kwa yani?
________________________________________(malikisi 1)

iii. Kodi mawu oti "galu wakuda" Akutanthauzanji?
________________________________________(malikisi 1)

b. Perekani njira imodzi yotumizira uthenga wa maliro m'mudzi.
________________________________________(malikisi 1)

c. Ndi yani amene ali ndi udindo wolangiza mfumu m'mudzi?

Candidate Name:________________________________________

________________________________________________________________________(malikisi 1)

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. Chidwi____________________________________________________________(malikisi 2)

b. Muliri____________________________________________________________(malikisi 2)

c. Achisozera________________________________________________________(malikisi 2)

d. Sema______________________________________________________________(malikisi 2)

e. Wanu______________________________________________________________(malikisi 2)

**GAWO B (malikisi 40)**

**Mafunso 6 mpaka 10**. Sankhani mawu omwe akusonyeza zambiri za mawu omwe ali m'munsiwa

6. Munda
   A. Minda C. Maminda
   B. Yiminda D. dziminda
7. Nthenda
   A. Chithenda C. Vimatenda
   B. Matenda D. Timatenda
8. Kapolo
   A. Makapolo C. Tiakapolo
   B. Zikapolo D. Akapolo
9. Dziko
   A. Maiko C. Maziko
   B. Dziko D. dzimaiko
10. Chikwama
   A. Dzikwama C. zikwama
   B. Makwama D. chikwama

**Mafunso 11 mpaka 15** sankhani maina a zinthu zokhuzika m'ziganizo zotsatirazi

11. Iwo adagwa pampando wa sofa
   A. Mpando C. Adagwa
   B. Iwo D. Wasofa
12. Ulimi waziweto ndi wabwino.
   A. Ulimi C. Ziweto
   B. Wabwino D. Ndi
13. Bzalani mitengo yambiri kuno.
   A. Bzalani C. Kuno
   B. Mitengo D. yambiri
14. Mankhwala amachiza matenda osiyanasiyani
   A. Amachiza C. Osiyansiyana
   B. Matenda D. Mankhwala
15. Edzi imafala podzera m'chiwerewere ndi malezala.
   A. Malezala C. Imafala
   B. Edzi D. Chiwerewere

**Mafunso 16 mpaka 20.** Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro za m'kalembedwe zoyenera m'ziganizo zotsatirazi.

16.
   A. Mbale zili mbwe! pabwalo.
   B. Mbale ziri mbwe Pabwalo.
   C. Mbale, ziri mbwe Pabwalo.
   D. Mbale! ziri mbwe pabwalo.

17.
   A. Taphunzira kuti Malungo ndi oopsa
   B. Taphunzira kuti malungo ndi oopsa.
   C. Taphunzira, kuti malungo ndi oopsa
   D. Taphunzira kuti, Malungo ndi oopsa.
18.
   A. Nasiwande adati, amenewo ndi maganizo abwino
   B. "Nasiwande adati, " amenewo ndi maganizo abwabwino.
   C. Nasiwande adati, "amenewo ndi maganizo abwino."
   D. Nasiwande adati amenewo ndi maganizo abwino.
19.
   A. Chifukwa cha njala iye adamwa zakumwa zonse.
   B. Chifukwa cha njala iye, adamwa zakumwa zonse.
   C. Chifukwa cha njala iye adamwa, zakumwa zonse.
   D. Chifukwa cha njala, iye adamwa zakumwa zonse.
20.
   A. Kodi mnkhaniyi, mwaphunziramo chiyani?
   B. Kodi m'nkhaniyi mwaphunziramo chiyani?
   C. Kodi mn'khaniyi mwaphunziramo chiyani?
   D. Kodi m'nkhaniyi, mwaphunziramo chiyani?

**Mafunso 21 mpaka 25:** sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

21. Ndagula msomba <u>ndi</u> nyama lero
   A. Mneni C. Dzina
   B. Muonjezi D. Mlumikizi
22. <u>Iye</u> akuti sapita nawo ku maliro.
   A. Mlowammalo C. Mfotokozi
   B. Dzina D. Mneni

23. Chimwemwe wapita ku maliro.
    A. Mlowammalo C. Mfotokozi
    B. Mperekezi D. Muonjezi
24. Nkhuku yamawanga ija yasowa.
    A. Mneni C. Mlowammalo
    B. Mfotokozi D. Mperekezi
25. Jakobo walephera mayeso.
    A. Mneni C. Mmlowammalo
    B. Dzina D. Mfotokozi

**Mafunso 26 mpaka 29.** Sankhani mawu oyenera kutsirizira zifanifani zotsatirazi

26. Kuda ngati ______________.
    A. Njinga C. Ufa
    B. Makala D. Tala
27. Kupusa ngati _____________.
    A. Mlamba C. Chule
    B. Mbuzi D. Nkhosa
28. Kuyabwa ngati _________________
    A. Tsabola C. Madzi
    B. Chitedze D. Mafuta
29. Kuchenjera ngati __________________
    A. Gaba C. Mkango
    B. Kalulu D. Namzeze

**Mafunso 30 mpaka 34.** Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa.

30. Mbulanda
    A. Sauka C. Vala
    B. Maliseche D. Nyanda
31. Mtudzu
    A. Mwano C. Wawa
    B. Chimbudzi D. Makani
32. Mbwani
    A. Chinangwa C. Mbatata
    B. Nandolo D. Khobwe
33. Dondo
    A. Kumanda C. Nkhalango
    B. Kumudzi D. Kuchipinda
34. Masano
    A. Dondo C. Thengo
    B. Kumanda D. Masana

**Mafunso 35mpaka 39.** Sankhani chaching'ono cha zinthu izi:

35. Nkhuku
    A. Mphonda C. Kankhuku
    B. Mwanapiye D. Tambala
36. Mayi
    A. Mzimayi C. Mtsikana
    B. Mayi D. Azimayi
37. Nkhunda
    A. Maunda C. Mphonda
    B. Mwanapiye D. Chiunda
38. Chule
    A. Mbiriwidzi C. Kachule
    B. Achikulire D. Khanda
39. Bambo
    A. Mdala C. Mnyamata
    B. Achikulire D. Mzibambo

**Mafunso 40 mpaka 44,** Perekani mayankho a ndagi kapena zilapi izi.

40. Amayi tsalani, kunyumba ndipita ndekha.
    A. Chimanga C. Nandolo
    B. Nthochi D. Chigwada
41. Mfuti yanga yolasira kumbuyo.
    A. Uta C. Njuchi
    B. Nsomba D. Minga
42. Ndimati nchiponde koma chaponda ine.
    A. Madzi C. Chithunzi
    B. Mchenga D. Nsapato
43. Ndili ndi ng'ombe zanga zakuda kwambiri.
    A. Makala C. Dothi
    B. Midzodzo D. Anthu
44. Alira atazimenya yekha.
    A. Mariya C. Belu
    B. Nthochi D. Tambala

**Mafunso 45 –46** Tsirizani mukuluwiko yotsatirayi ndi mawu oyenera.

45. Walira mvula walira_____________.
    A. Sukulu C. Matope
    B. Nyama D. madzi
46. Ulenje umasimba____________.
    A. Wako C. Wanga
    B. Wanu D. Wathu

# MAFUNSO ATHERA PA TSAMBA LINO